# PHUNZIRO 48

1.Kodi Yesu anachimwako?
-Iyayi.

2. Kodi chifukwa chiyani Yesu anamŵera lamulo lina lililonse la Mulungu, ndiponso sanachimwe? -Chifukwa chakuti Yesu sanabadwire mu tchimo.

3. Kodi chifukwa chiyani Yesu sanabadwire mu tchimo?
-Chifukwa chakuti Yesu analibe mbewu ya bambo wa umunthu.
-Chifukwa chakuti Yesu analibe mbewu ya mayi wa umunthu.
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu.

4. Kodi pali munthu amene alibe tchimo ngati Yesu.
-Palibe.
-Anthu onse anabadwira mu tchimo.

5. Kodi Yesu ankachita chiyani pamene Yosefe ndi Mariya anamupeza Iye ali M'kachisi wa Mulungu ku Yelusalemu?
-Yesu ankaŵam'vera aphunzitsi a mawu a Mulungu akuphunzitsa komanso kumaŵafunsa mafunso.
-Yesu ankaphunzitsanso mawu a Mulungu kwa ophunzitsa mawu a Mulungu.

6. Kodi Yesu ankaŵadziŵa bwanji mawu a Mulungu pamene Iye anali ndi zaka 12?
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu.

7. Kodi Mariya atamufunsa Yesu, Yesu anayankha chi-
yani?
-Yesu anati, “Kodi simumadziŵa kuti ndiyenera
kupezeka Mnyumba ya Atate Anga a kumwamba?

8. Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani?
-Yesu ankatanthawuza kuti Iye ankachita zimene
Mulungu Atate ankafuna kuti Iye adzichita.

9. Kodi Yesu ankamumvera Yosefe ndi Mariya pame-
ne ankakula?
-Inde.

10. Ngakhale kuti Yesu ankawoneka ngati ana ena on-
se, kodi Yesu ankasiyana bwanji ndi ana enawo?
-Yesu anali Mulungu.
-Yesu anali Mulungu weniweni komanso mundu weni-
weni.

-Mulungu anapereka mwana wamamuna kwa Zakari-
ya ndi Elizabeti ndipo anamutcha dzina lache Yohane.

-Mwana wamamuna wa Elizabeti ndi Zakariya an-
katchedwa kuti Yohane.

-Mulungu anamutumiza Yohane M’batizi kudzaŵachita
Ayuda kukhala okonzeka m’mitima mwawo.

-Kodi Yohane M’batizi ankaŵachita Ayuda kukhala ok-
ozekera ndani m’mitima mwawo?
-Yesu Mpulumutsi.

-Kodi Yohane M’batizi ankayikomzekeretsa bwanji



-Kodi Yesu anali bwanji Mwana wa Mulungu Atate?
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu amene
anachoka kumwamba kudzachita zimene Atate ache
anafuna kuti Iye achite.

-Kodi Mulungu Atate analankhula chiyani za Yesu?
-Mulungu Atate analankhula kuti Iye ali osangalala
kwambiri ndi Yesu.

-Kenako Yohane M’batizi anamuwonanso Yesu.

-Apa pali zimene analankhula Yohane M’batizi za-
kumutcha Yesu:

Tiyeni tiŵerengeYohane 1:29

29-M’maŵa mwache Yohane anamuwona Yesu
akubwera kwa Iye, nanena kuti, “Onani Mwana wa
Nkhosa wa Mulungu, amene amachotsa tchimo la pa
dziko la pansi!”

-Yohane M’batizi anamutcha Yesu kuti “Mwana wa
Nkhosa.”
-Kodi chifukwa chiyani Yohane M’batizi anamutcha
Yesu kuti “Mwana wa Nkhosa?”
-Mulungu anamupereka Yesu kuti adzaŵafere anthu
onse ngati m’mene anaperekera mwana wa nkhosa
kuti afe m’malo mwa Isaki.

-Mulungu anamupereka Yesu ndi magazi ache kuti
adzaŵapulumutse anthu onse ngati m’mene zinafera
nkhosa ndi magazi ache kuti aŵapulumutse a Isirayeli.

-Chifukwa chakuti Yesu ankafuna kuwonetsa kuti Iye anali Mpulumutsi ndiponso olungama wa Mulungu.
-Chifukwa chakuti Yesu ankafuna kuwonetsa kuti maphunzitso a Yohane M'batizi anali ochokera kwa Mulungu.
-Chifukwa chakuti Yesu ankafuna kuwonetsa chitsanzo chabwino kwa nthu onse.
-Chifukwa chakuti Yesu ankafuna kuti amumvere Mulungu Atate mu zonse.

-Yesu anali Mulungu weniweni.

-Koma Yesu ankafuna kumumvera Mulungu Atate mu zonse.

-Chomcho Yesu anamupempha Mulungu Mzimu Oyera kuti amutsogolere Iye pamene adzikhale pa dziko la pansi.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 3:16-17

16-Ndipo Yesu anabatizidwa, pomwepo anaturuka m'madzimo. Nthaŵi yomweyo kumwamba kunatseguka, ndipo anawuwona Mzimu wa Mulungu ukutsika ngati nkhunda ndikutera pa Iye.
17-Ndipo Mawu anamveka kuchokera kumwamba akuti, "Uyu ndiye Mwana Wanga Wokondedwa, mwa Iyeyu ndikondwera."

-Mulungu Atate analankhula kuchokera kumwamba.

-Mulungu Atate anamutcha Yesu kuti Mwana Wache.



mitima ya Ayuda?
-Poŵaphunzitsa iwo Mawu a Mulungu.

-Mulungu anamusankha Yohane M'batizi kuti aŵaphunzitse Ayuda.

-Tsopano inali nthaŵi yakuti Yohane M'batizi ayambe kuphunzitsa.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 3:1-2

1-Pa masiku amenewo, Yohane anabwera ndikuyamba kulalikira m'chipululu cha ku Yudeya,
2-ndipo ankati, "Lapani mitima yanu pakuti Mulungu watsala pang'ono kuwukhazikitsa ufumu wache.."

-Kodi Yohane M'batizi ankaŵaphunzitsa chiyani anthu?
-Yohane M'batizi ankaŵaphunzitsa Ayuda kuti atembenuke mitima yawo ku machimo.

-Kodi kutembenuka mtima ku machimo kumatanthawuza kuti chiyani?
-Kutembenuka mtima kumatanthawuza kusintha maganizo athu pa Mulungu , ife ndi tchimo.

-Kutembenuka mtima kumatanthawuza kusintha maganizo athu pa Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu amafuna kuti ife tisinthe maganizo athu pa za Iye?

-Chifukwa chakuti ife timaganiza kuti tidzatha kukafika kwa Mulungu mu njira zathu.

-Kodi ife tingathe kukafika kwa Mulungu mu njira yathu?
-Iyayi.

-Mulungu ndi oyera ndipo ife tingathe kukafika kwa Mulungu mu njira ya Mulungu yekha.

-Kutembenuka mtima kumatanthawuza kusintha maganizo athu pa za Mulungu, pakuti Mulungu ndi oyera chomcho angathe kufukiridwa ndi njira imodzi yokha.

-Kutembenuka mtima kumatanthawuza kusintha maganizo athu pa za ife pakuti tamchimwila Mulungu.

-Yohane M'batizi anaŵaphunzitsa Ayuda kuti iwo akuyenera kutembenuka mitima yawo ku machimo.

-Izi ndi zimene analankhula Mneneri Yesaya za Yohane M'batizi.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 3:3

3-Yohane ndi Mneneri amene analankhulidwa ndi Yesaya pamene ankati kuti, "Munthu wina akufuwula m'chipululu, ndipo akuti," "Konzani njira yodzera Ambuye; ongolani njira zachezo."

-Mneneri Yesaya analankhula kuti Yohane M'batizi anali munthu amene adzabwere kudzatembenuza anthu mitima pa kubwera kwa Mpulumutsi.



vomereza kuti iwo amulakwila Mulungu. Adzaŵawotcha ngati zotsalira (gaga) mu nyanja ya moto osatha.

-Tsiku lina Yesu anafika kwa Yohane kuti abatizidwe ndi iye.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 3:13-15

13- Kenako Yesu anabwera ku Yolodani kuchokera ku Galileya kuti abatizidwe ndiYohane.
14-Koma Yohane anayesa kumukana Iye polankhula kuti, "Ine ndili oyenera kubatizidwa ndi Inu, komanso Inu mukubwera kwa ine?"
15-Yesu anayankha kuti, "Tiyeni tizisiye kuti zikhale chomcho tsopano; kuli koyenera kwa ife kuti tikwaniritse chilungamo chonse motero. " Kenako Yohane analora.

-Kodi chifukwa chiyani Yohane M'batizi anamubatiza Yesu?
-Kodi chinali chifukwa chakuti Yesu anatembenuka mtima?
-Iyayi.

-Kodi kapena Yesu ankafuna kuti atembenuke mtima?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu sankafuna kuti atembenuke mtima?
-Chifukwa chakuti Iye sanachimweko.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Yohane M'batizi anamubatiza Yesu?

mula. Iye adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto."

-Pamene Yohane M'batizi ankaŵabatiza anthu ndi madzi, iye anati kuti Yesu Mpulumutsi adzidzaŵabatiza anthu ndi Mzimu Woyera.

-Yohane M'batizi analankhulanso kuti Yesu Mpulumutsi anali Mulungu oyera kwambiri amene iye sanakatha kunyamula nsapato Zache.

-Kodi china chiyani chimene analankhula Yohane M'batizi za Yesu Mpulumutsi?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 3:12

12-[Yohane M'batizi analankhulanso kuti] "M'manja mwache muli chopetela kuti apete tirigu wache, ndipo adzathira tirigu mu nkhokwe yache, koma zotsalira (gaga) adzadziwotcha pa moto wosazimitsidwa."

-Yohane M'batizi analankhula kuti anthu onse amene akudzikweza ndi kukana kuvomereza kuti iwo amuchimwira Mulungu, ali ngati zotsalira za tirigu (gaga wa Tirigu).

-Kodi gaga ndi wabwino pa chiyani?
-Palibe.
-Ndi wabwino pomuwotcha.

-Yohane M'batizi analankhula kuti Yesu Mpulumutsi adzaŵawotcha anthu odzikweza amene akukana ku-



-Ngakhale kuti Yohane M'batizi anali Mneneri wa Mulungu, anali osawuka.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 3:4

4-Yohane ankavala zovala za chikopa cha ngamila, ndipo ankamangiranso lamba wa chikopa mchiwunu mwache. Zakudza zache zinali dzombe ndi uchi wa mthengo.

-Zovala za Yohane M'batizi zinapangidwa ndi chikopa cha ngamila.

-Yohane M'batizi ankadya dzombe ndi uchi wa mtchire.

-Anthu ena amaganiza kuti Mulungu adzaŵapatsa iwo ndalama zambiri akamakhulupilira mwa Iye.

-Koma Mulungu samapereka lonjezo la ndalama zilizonse kwa munthu aliyense.

-Chifukwa chakuti Yohane M'batizi ankaphunzitsa zinthu zambiri za Mulungu, Ayuda ambiri ankabwera kwa iye.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 3:5-6

5-Anthu ochokera ku Yerusalemu ndi dziko lonse la Yudeya, ndiponso mbai zonse zoŵandikana ndi mtsinje wa Yolodani, ankabwera kwa iye.

6-Iwo amkati akalapa machimo awo, iye ankaŵabatiza mu mtsinje wa Yolodani.

-Ayuda ambiri anakhulupilira mawu a Mulungu kudzera mwa Yohane M'batizi.

-Ayuda ameneŵa anavomereza machimo awo pa maso pa Mulungu, ndipo anamupempha Mulungu kuti aŵapulumutse iwo.

-Chifukwa chakuti Ayuda ameneŵa anaŵavomereza machimo awo pa maso pa Mulungu, ndikumupempha Mulungu kuti aŵapulumutse, Yohane M'batizi ankaŵabatiza.

-Kodi ubatizo ndi chiyani?
-Ubatizo ndikumuvika munthu m'madzi ndikumuvuwulanso mwamsanga.

-Kodi ubatizo umatanthawuza chiyani?
-Ubatizo ndi chidziŵitso chakuti inu mwavomereza machimo anu pa maso pa Mulungu, ndipo mukumupempha Mulungu kuti akupulumutseni.

-Kodi ubatizo unatha kuŵapulumutsa Ayuda ku mphamvu ya sambi, imfa ndi Satana?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani ubatizo siwunathe kuŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya sambi, imfa ndi Satana?
-Chifukwa chakuti kuŵavika anthu m'madzi, sikungathe kuŵapulumutsa anthu.



-Kodi tikaphophola zipatsa mu mtengo oyipa, kodi mtengowo ukafuna kuberekanso, ungabereke zipatso zabwino?
-Iyayi.

-Mtengowo udziberekabe zipatso zoyipa nthaŵi zonse.

-Ngati tikudula nthambi za mtengo oyipa, kodi mtengowo ungamelenso nthambi zina zabwino?
-Iyayi.
-Mtengowo udzimerabe nthambi zoyipa nthaŵi zonse.

-Ife tonse tili ngati mtengo abereka zipatso zoyipa.

-Palibe chinthu chimene ife tingachite kuti tidzichite kukhala ngati anthu abwino.

-Ngati tikudzikweza ndikumakana kuvomereza kuti ife tamchimwira Mulungu, Mulungu adzatidula ife ngati mtengo obereka zipatso zoyipa ndikutiponya ife mnyanja ya moto osatha.

-Kenako Yohane M'batizi analankhula za Yesu Mpulumutsi.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 3:11

11-[Yohane M'batizi analankhulanso kuti] "Ine ndikukubatizani inu ndi madzi kuwonetsa kutembenuka mitima . Koma pambuyo panga abwera wina amene adzakhala ndi mphamvu kupambana ine. Amene ngakhale nsapato zache sindingathe kunya-

Mulungu akhoza kuyichita miyalayi kukhala ana a Abulahamu.”

-Yohane M’batizi analankhula kuti ngakhale kuti Afarisi ndi Asaduki anali zidzukulu za Abulahamu, zimenezo sizingatheke kumusangalatsa Mulungu.

-Kodi kukhala chidzukulu cha munthu wina wache, kungamupangitse Mulungu kusangalala ndi ife?
-Iyayi.

-Yohane M’batizi analankhula kuti Mulungu anakatha kupanga zidzukulu za Aburahamu kuchokera ku miyala anakafuna kupanga chomcho.

-Kodi china chiyani chimene analankhula Yohane M’batizi kwa Afarisi ndi Asaduki?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 3:10

10-[Yohane M’batizi analankhulanso kuti] “Nkhwangwa yayikidwa kale pa phuthu la mtengo, ndipo mtengo uliwonse osabereka zipatso uyenera kudulidwa ndikuponyedwa pa moto.”

-Kodi Yohane M’batizi analankhula chiyani za anthu onse amene ali odzikweza ndipo okana kuvomereza kuti iwo anamulakwira Mulungu?
-Analankhula kuti Mulungu adzaŵadula iwo ngati mtengo osabereka ndi kuŵaponya mnyanja ya moto osatha.

-Apa pali chitsanzo:



-Kodi ubatizo ungathe kumupulumutsa munthu aliyense ku mphamvu ya sambi, imfa ndi Satana?
-Iyayi.

-Ubatizo siwungathe kutipulumutsa ife ku mphamvu ya sambi, imfa ndi Satana.
-Ubatizosiwungathe kuyeretsa sambi zathu.
-Ubatizo siwungathe kulipira sambi zathu.

-Kodi ndani yekha amene anakatha kuŵapulumutsa Ayuda ku mphamvu ya sambi, imfa ndi Satana?
-Yesu Mpulumutsi.

-Ubatizo ndi chidziŵitso chakuti inu mwavomereza machimo anu pa maso pa Mulungu ndipo mukumupempha Mulungu kuti akupulumutseni.

-Afarisi ndi Asaduki ambiri nawonso anafika kukamumvera Yohane M’batizi.

-Kodi Yohane M’batizi analankhula chiyani kwa Afarisi ndi Asaduki?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 3:7

7-Ayuda ambiri a m’maguru a Afarisi ndi Asaduki, nawonso ankabwera kwa iye kudzabatizidwa, koma Yohane ataŵawona iwo anati, “Ana a njoka inu, kodi ndani amene wakuchenjezani kuti muchithaŵe chilango cha Mulungu chimene chikubwerachi?”

-Yohane M’batizi anaŵatcha Afarisi ndi Asaduki kuti ndi ana a njoka.

-Kodi chifukwa chiyani Yohane M’batizi anaŵatcha Afarisi ndi Asaduki kuti ndi ana a njoka?
-Chifukwa chakuti Afarisi ndi Asaduki anali odzikweza kwambiri.
-Chifukwa chakuti Afarisi ndi Asaduki sanavomereze kuti iwo anali ochimwa kwa Mulungu.

-Mawu a Yohane M’batizi anali amphamvu kwambiri kwa Afarisi ndi Asaduki.

-Izi zinali chomcho chifukwa chakuti Afarisi ndi Asaduki anali odzikweza kwambiri, ndiponso sankavomereza kuti iwo anamulakwira Mulungu.

-Mulungu sadzaŵapulumutsa anthu adzikweza ndipo osavomereza kuti amulakwira Mulungu.

-Mulungu adzaŵapulumutsa anthu amene ali osadzikweza ndipo amene avomereza kuti amulakwira Mulungu.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Yohane M’batizi kwa Afarisi ndi Asaduki?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 3:8

8-[Yohane M’batizi analankhulanso kuti] “Muziyang’anitsitse nokha ndi ntchito zanu kuti mwatha kutembenuka mitima.”



-Afarisi ndi Asaduki ankaganiza kuti Mulungu ankasangalala ndi iwo.
-Kodi chifukwa chiyani Afarisi ndi Asaduki ankaganiza kuti Mulungu ankasangalala ndi iwowo?
-Chifukwa chakuti iwo ankaganiza kuti ntchito zawo zingathe kumupangitsa Mulungu kusangalala.

-Kodi ntchito zimene timapanga zingathe kumupangitsa Mulungu kusangalala ndi ife?
-Iyayi.

-Yohane M’batizi analankhula kuti ntchito imene ingamusangalatse Mulungu ndi yotembenuka ku machimo yokha.

-Ntchito imene ingamusangalatse Mulungu kwa munthu aliyense ndi yotembenuka ku machimo yokha.

-Kodi chifukwanso chiyani chimene ankaganiza Afarisi ndi Asaduki kuti Mulungu ankasangalala ndi iwo?
-Afarisi ndi Asaduki ankaganizanso kuti Mulungu anali osangalala ndi iwo chifukwa chakuti iwo anali zidzukulu za Abulahamu.

-Kenako, kodi Yohane M’batizi analankhula kuti chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 3:9

9-[Yohane M’batizi analankhulanso kuti] “Ndipo musamayese kudzikweza nokha ponena kuti, “Tinali ndi Abulahamu ngati tate wathu.” Ndikukuwuzani kuti